# ATUMIKI A BAPTIST:
# KUTUMIKIRA NDI CITSANZO



LOLEMBEDWA NDI JERRY HUBBARD

# ATUMIKI A BAPTIST: KUTUMIKIRA NDI CITSANZO

**Linalembedwa ndi: Bambo Jerry Hubbard**

**BAPTIST DEACONS: MINISTRY BY EXAMPLE**

*(Chinyanja)*

*Published by*
*Baptist Publishing House*
*P.O. Box 31995, 10101*
*Lusaka, Zambia*

*Printed by*
*Baptist Printing Ministry*
*P.O. Box 31995, 10101*
*Lusaka, Zambia*

©Copyright, 2011,
International Publications Services
All Rights Reserved
www.ipsimb.com
ipsid: bd_mbe-zam-nya

## Za Mkatimu

**MUTU** **TSAMBA**

**GAWO LOYAMBA:** Zofunikira Mtumiki
1. Mtumiki ndi Munthu wa Uzimu ........ 7
2. Mtumiki ndi Munthu wa Makhalidwe Abwino ........ 8

**GAWO LACIWIRI:** Atumiki: Kutumikira pa Kuonetsa Citsanzo ........ 11
3. Mtumiki Kutumikira Pakukhala Citsanzo Mukaphunzitsidwe Kakukula mu Uzimu ........ 13
4. Mtumiki Athandizira pa Kupatsa Citsanzo Cakhalidwe la Moyo Wace ........ 15
5. Mtumiki Atumikira pa Kukhala Citsanzo pa Khalidwe la Banja Lace ........ 18
6. Mtumiki Athandizira pa Kukhala Acitsanzo mu Dziko la Malonda ........ 20
7. Mtumiki Athandizira pa Kukhala Citsanzo ku Malo Kumene Agwira Nchito ........ 21
8. Mtumiki Kukhala Citsanzo pa Kubvomereza Udindo wa Utsogoleri wa za Uzimu ........ 22
9. Atumiki Atumikira pa Kukhala Citsanzo pa Kuyendera Mamembala Atsopano mu Mipingo ........ 24
10. Mtumiki Atumikira pa Kukhala Citsanzo Mukucitira Umboni ........ 25
11. Mtumiki Amatumikira pa Kukhala Citsanzo pa Kuthandizira Mbusa ndi Zocitika za Uzimu Kuthandizira pa Mpingo ........ 27

**GAWO LACITATU:** Kusankha ndi Kudzoza Kwa Atumiki
12. Kudzoza: Zikhulupiriro ndi za Kucita a Baptist ........ 31
13. Kusankha kwa Atumiki ........ 34
14. Kudzoza kwa Atumiki ........ 36

## Mndandanda Waciwiri

Kufika kwa anthu ndi kuimba kwa amaimbidwe

Nyimbo ya m'buku

Pemphero

Nyimbo ya m'buku

Kulandira alendo ndi kudziwa komwe acokera

Kudziwitsa atumiki amene adzadzozedwa ndi amene anali mu bungwe loyesa akudzozedwa, zocokera kwa akumpando wa bungwe loyesa akudzozedwa

Nyimbo za padera

Mau ku atumiki ndi mpingo

Kuika manja - Atumiki onse amene akali kutumikira mwa mphamvu amene ali odzozedwa kale ndi azibusa a mipingo ya Baptist

(Atumiki amene adzozedwa adzagwada kutsogolo kwa anthu ndipo akazi kapena amuna awo adzaimirira kumbuyo kwao.)

Mamembala a mpingo apereke moni wa kubvomereza kudzoza

Pemphero la kupereka atumiki adzozedwa kwatsopano m'manja ya Mulungu

Kupeleka mapepala kwa omwe adzozedwa (masetifiketi)

Kupeleka mphatso ndi kuyamikira - anthu onse

Pemphero lomaliza

Zakumwa ndi kupita

Zotsatira ndi zitsanzo ziwiri za mindandanda imene ingagwiritsidwe nchito monga zotsatira pamene tikonzekera msonkhano wa kudzoza atumiki.

**Mndandanda Woyamba**

Kufika kwa anthu ndi kuimba kwa amaimbidwe

Nyimbo ya m'buku

Pemphero

Kulandira alendo ndi kudziwa komwe acokera

Kubvomereza kucokera ku akumpando a bungwe la oyesa akudzozedwa

Nyimbo ya padera

Mau ku atumiki

Kuika manja - atumiki onse amene ali odzozedwa ndipo akali kutumikira mwa cangu pamodzi ndi azibusa a mipingo ya Baptist

(Atumiki amene adzozedwa adzagwada kutsogolo kwa anthu ndipo amuna awo kapena akazi awo adzaimirirakumbuyo kwao.)

Pemphero ya kupereka atumiki amene adzozedwa kwatsopano

Kupeleka mapepala (masetifiketi) kwa adzozedwa ndi wa kumpando wa bungwe la oyesa

Kupeleka mphatso ndi kuyamika - Anthu onse

Pemphero lomaliza

Zakumwa ndi kupita.



# GAWO LOYAMBA

## ZOFUNIKIRA MTUMIKI

Kuli anthu ena amene anapemphedwa ndi mpingo wao kuti atumikire monga atumiki. Kucotsako mbusa, palibe mtsogoleri wina mu mpingo ali opambana mtumiki.

Ngakhale kuti ambiri atumikira monga atumiki mu mipingo yao msokonezo ukalipobe pa za atumiki. Cobweretsa msokonezo ndi cakuti mtumiki ndani? Nanga nchito yace ndi yotani?

Malembo amatipatsa zofunikira za uzimu ndi zakhalidwe la mamembala a mpingo amene asankhidwa ndi mipingo yao kutumikira mu utsogoleri wa utumiki. Izi zofunikira siziyenera kutengedwa mwa masowera cifukwa (1) ndi zopatsidwa ndi Mulungu kupyolera mwa malembo kuti mpingo utsatire mosalephera. (2) Malo a utsogoleri wa utumiki afunika kukula kweni-kweni mu uzimu ndi umoyo wabwino kumbali ya munthu amene abvomera malo awa a utsogoleri mu mpingo ndi (3) zofunikira zonse zimene ziri zofunikira pang'ono kuposa za uzimuzi ndi za umoyo zingaonetse khalidwe la uzimu ndi umoyo wa Mulungu amene amadzionetsera **yekha monga Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera.**

ca mphatso ya akapolo mu mpingo amene atsatira zitsanzo za Yesu, kapolo wa akapolo. Ngati nthawi siiri nthawi ya kupembedza, ndiye kuti ndi nthawi yolemekeza munthu m'malo molemekeza Ambuye Mulungu wathu, Yesu Kristu.

kotero kuti akonzekere bwino gawo lao. Pamene tsiku la kudzoza liikidwa, makalata akuitana mipingo ina, olalikira, amaimbidwe, ndi anthu ena atumidzidwa mwamsanga.

Mwina tiyenera kutsimikiza fundo iyi yokhuza amene ayenera kudzoza mtumiki. Ena amaona monga guru loyesa liri monga guru la odzoza. Ici sicoona ai. Guru loyesa ndi guru lothandizira kuyesa atumiki amene afunika kuti adzozedwe ndi kubweretsa ku mpingo zimene apeza ndiponso kubweretsa ganizo lao ku mpingo kuyesa kutatha. Akumpando abungweli adzabweretsa zimene agwirizana ndi amene ayankha mafunso moyenera ku mpingo kuti adzozedwe. Kupereka zimene anapeza amazibweretsa ku mpingo pa nthawi kapena tsiku la kudzoza. Motero, ndi mpingo wa okhulupirira kumene atumiki acokera, umene umadzoza atumiki.

Mpingo umaonetsa poyera kupyolera pa kudzoza cikhulupiriro cao cakuti anthu amene adzozedwa aonetsa kuti ali okula mu utsogoleri wa uzimu mu mpingo ndi mzocitika zonse za uzimu za pa mpingo. Mpingo uli kunenanso poyera kuti okhulupirira amene adzozedwa adzapitirira kuonetsa kukula kwao mu utsogoleri wa uzimu ndi kukula pamene agwira nchito monga akapolo mu utumiki wao. Kudzoza ndi citsimikizo ca odzozedwa kuti aona ndi kumvetsetsa nchito yao kukhala ya kutumikira. Ndi nchito ya ukapolo, osati ya mphamvu ndi ulamuliro pa mpingo wonse.

Mpingo uitana anthu odzodzedwa kucokera ku mipingo ina ya Baptist kutenganso mbali mukudzoza pa kuika manja pa mutu wa odzozedwa pa nthawi ya kudzoza. Kuika kwa manja kwa akapolo anzao amene anadzozedwa sikupatsa mphamvu ya padera ku odzozedwayo. Kuika kwa manja pa mutu ndi nthawi ya padera pamene akapolo ena odzoza apereka mapemphero amadalitso ndi kupempherera zipatso mu nchito ya atumiki anzao amene adzozedwa ndi mpingo. Mwina payenera kukhala mpata ku mamembala a mpingo umene udzoza atumiki kudza kutsogolo ndi kutenganso mbali pa zocitika pakuti ndiye mpingo udzoza atumiki osati guru loyesa lija kapena anthu a mipingo ina ya Baptist amene anadzozedwa kale ai. Onani pa citsanzo ca mndandanda wa zocitika pa kudzoza pa masamba osatira.

Mpingo uli womasuka kukonza mndandanda monga ungafunire, komanso, mpingo uyenera kudzindikira kuti kudzoza coyamba-yamba ndi nthawi ya kupembedza Mulungu kupyolera mwa Yesu Kristu. Ndi nthawi ya kupembedza Mulungu cifukwa



## MUTU 1

## MTUMIKI NDI MUNTHU WA UZIMU

Coyambirira, mtumiki ndi munthu amene atenga khalidwe la Cikristu osati mwa masowera m'malo a umoyo wozikhalira. Mu Macitidwe 6:3 umoyo wa Kristu ufotokodzedwa monga "...odzala ndi Mzimu." Ici citanthauza kuti umoyo wa mtumiki ulamuliridwa ndi kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera monga momwe umoyo wa Yesu unali wolamulidwa ndi kutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera.

Mtumiki ndi munthu amene amagwiritsa nchito nzeru za uzimu pamene acita zinthu za mu mpingo ndi zokhudza mamembala a mu mpingo. Macitidwe 6:3 ilankhulanso kuti atumiki ayenera kukhala "odzala ndi nzeru amene tingawaike asunge nchito iyi." Pakuwerenga Macitidwe 6:3 cingaoneke kuti "nzeru" ili yogwirizana ndi "kudzazidwa ndi Mzimu Woyera." Ici cimationetsa ife mtundu wa "nzeru" atumiki ayenera kukhala nayo ndi kugwiritsa nchito mu utumiki wao. Ndi nzeru za uzimu. Nzeru izi ndi zoposa nzeru za umunthu. Mtumiki ndi munthu amene amalola nzeru za uzimu ndi kumvera kuti zikhala zopambana pa nzeru zace ndi kumvera kwace monga munthu.

"Okhala naco cinsinsi ca cikhulupiriro m'cikumbumtima coona" citanthauza kuti mtumiki ndi munthu amene ali ndi cikhulupiriro ca ciphunzitso ndi citsimikizo colamitsa. Siciyenera kunenedwa pa za mtumiki kuti ndi munthu amene "atengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya ciphunzitso" (Aefeso 4:14). Mtumiki ayenera kutenga cilimbikitso ca Paulo kwa akuru a mpingo a ku Aefeso motsimikiza: "Tadzicenjerani nokha, ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyang'anira, kuti muwete Eklesia wa Mulungu, umene anaugula ndi mwazi wa iye yekha" (Macitidwe 20:28).

## MUTU 2

### MTUMIKI NDI MUNTHU WA MAKHALIDWE ABWINO

Mtumiki ndi munthu wa mbiri yabwino pakati pa ciyanjano ca okhulupirira amene anamusankha iye kuti atumikire monga m'modzi wa atumiki ao. Mu Macitidwe 6:3 pempho locokera kwa atumwi ku ciyanjano ca okhulupirira a ku Yerusalemu cinali cakuti, "...yang'anani mwa inu amuna asanu ndi awiri ambiri yabwino." Lero "mbiri yabwino" itanthauza mbiri ya Cikristu. Mtumiki salankhula cabe za zikhulupiriro zace ndi zicitidwe zace, akhala motero tsiku ndi tsiku m'makhalidwe ndi m'zicitidwe zace. Mbiri yabwino ya Cikristu ikhale mu ciyanjano ca okhulupirira maka-maka pakati pa anthu akunja osakhulupirira.

Mtumiki ndi munthu amene ali odzipereka ku colinga ca Cikristu. Mu 1 Timoteo 3:8 Paulo, pa kunena za zofunikira atumiki, anati, "...atumiki akhale olemekezeka." Liu limene Paulo anagwiritsa nchito limamasulidwa "olemekezeka" linali ndi tanthauzo lakuya kwambiri kupambana masiku ano. Pamene munthu ali pamaso pa atumiki, munthuyo ayenera kumva ulemelero wa mtumiki pa zinthu za uzimu.

Mtumiki ndi munthu amene nthawi zonse ali waukhondo m'maganizo ndi wonena zoonadi. Paulo anati mu 1 Timoteo 3:8-9, "Momwemonso atumiki akhale...osanena pawiri...okhala naco cinsinsi ca cikhulupiriro m'cikumbumtima coona. Osanena pawiri citanthauza kuti wanena cinthu cina kwa munthu wina ndi kupita ndi kulankhula cina kwa munthu wina." Mtumiki ndi munthu amene asunga lilime lace m'malo mwa kulamulilidwa ndi lilime. Iye amalankhula cifukwa ca kufuna kucita cilungamo nthawi zonse kuposa kulankhula cifukwa ndi kofunikira kapena cakuti ndi nthawi yabwino ya kulankhula. Iye amalamulira ukali wace kapena kuti sakalipa cikalipe-kalipe. Nthawi zonse ali okhulupiririka pa zimene amalankhula. Tonzo, kulankhula zakumva cabe osati zimene waona, kulankhula mosasamala kapena kunyoza sizili mbali ya khalidwe la mtumiki.

Mtumiki ndi munthu amene satenga vinyo kukhala cakumwa. Akristu ku zaka zoyamba anali mboni zoona za khalidwe la uciwerewere wopitirira. Cimodzi ca kacitidwe ka uwerewere kunali kumwela vinyo dala kufuna kuyesa kuledzera. Kuledzera nthawi zonse kumatsogoza kuzicitidwe za cipongwe, kuyambana ndi uciwerewere.



ena a mu mpingo, m'mene amaganizira pa za nchito ya utumiki, ngati ndi udindo wa kukhala ndi mphamvu ya ulamuliro pa mpingo kapena ndi udindo wa kutumikira, njira zimene iwo ali kuonetsera cikhulupiriro cao pa banja lao, kumene agwira nchito, zimene amaganiza pa kutengako mbali pa nchito ya asosiyeshoni ndi zocitika za utumiki mu konveshoni ndi mafunso okhudza ulamuliro wa a Baptist ndi mwambo wao. Pakumaliza kwa mayeso oyesedwa kawiri-kawiri amapatsidwa mpata wakuti afunseko mafunso pa zinthu zimene samvetsetsa bwino pa ziphunzitso za a Baptist ndi zocita zao. Kakonzedwe kamayeso kayenera kukhala kakuti munthu woyesedwa ayenera kukhala womasuka pa nthawi ya kufunsidwa mafunso ndi ofunsa.

Guru la oyesa ili ndi ulamuliro wa kupereka ganizo imodzi kapena awiri. Coyamba, guruli lingabvomereze ku mpingo kuti munthu amene wayesedwa adzozedwe monga mtumiki mu mpingo kapena, caciwiri, angabweretse ganizo lakuti munthu amene woyesedwa sayenera kuti adzozedwe monga mtumiki mu mpingo. Guruli limabweretsa ganizo lotere pamene munthu wofunsidwa alephera kupatsa mayankho yofunikira kufunso ndipo wofunsa aona kuti munthu uja sali wokonzeka kuti akhale ndi nchito ya utumiki.

Anthu oyesedwa amauzidwa za ganizo la oyesa nthawi ya kudzoza lisanafike. Angauzidwe za ganizo la oyesa (1) pamenepo atamaliza mayeso, (2) pakulembeledwa kalata kucokera ku wakumpando wa oyesa kapena (3) kupyolera mwa mbusa wa mpingo amene wapatsidwa ganizo la oyesa lolembedwa la munthu aliyense amene anayesedwa. Mbusa amene afuna kuti atumiki ace adzozedwe kawiri-kawiri amapemphedwa kuti apezekeko kukhala ndi guru loyesa pa nthawi la kuyesa, ngakhale kuti sali m'modzi wakuikapo ganizo. Iye amakhala ngati munthu wofufuzako ngati oyesa afuna kutero.

Ndi nchito ya mpingo kuika tsiku la kudzoza atumiki. Mpingo uli ndi nchito ya kudziwitsa a m'guru loyesa ndi mipingo ina za tsiku la kudzoza atumiki. Ndi nchitonso ya mpingo kukonza mndandanda wa zocitika pa kudzoza. Anthu amene adzakhala ndi zocita pa za kudzoza apemphedweretu nthawi ikalipo yokwanira kuti akonzekere gawo lao mu mndandanda ndi kuti akonze zocita zina kuti akapezeke pa kudzoza. Ngati amaimbidwe ocokera ku mpingo wina wa Baptist unapemphedwa kuti akaimbe nyimbo ya padera pa tsiku la kudzoza, pomwepo amaimbidwe ayenera kuuzidwa ndi kupatsidwa nthawi yokwanira

MUTU 14

## KUDZOZA KWA ATUMIKI

Kudzoza kwa atumiki kumatsatira mwambo wa kusankha. Anthu amene asankhidwa ku nchito iyi ya utsogoleri adzayenera kuphunzitsidwa nchito yao ya utumiki kuti akakhoze mu nchito yao ya utumiki. Iwo amene angaphunzitse atumiki atsopano ndi: mbusa wa pa mpingo omwewo; mbusa wina wa mpingo wa Baptist, mkuru wa mpingo, atumiki ena amene adziwa bwino nchito ya utumiki mu mpingo wa cimishoni wothandizira mpingo kuti ukule kapena wa cimishoni wina kapena wogwira nchito ku Baptist Konveshoni ya Zambia monga wa cimishoni, mphunzitsi wa pa sukulu la ubusa kapena ena.

Maphunziro awo ayenera kukhala ndi nkhani izi: zoyenera za atumiki za mu Cipangano Catsopano, kuonanso pa nchito ya atumiki asanu ndi awiri mu mpingo ku Yerusalemu; kuonanso cifukwa ciani mpingo wa mu Yerusalemu unasankha atumiki oyamba; mgwirizano pakati pa mtumiki ndi mpingo, abusa, banja, anthu omuzungulira ndi atumiki anzace; kuonanso pa nchito ya atumini mu mpingo ndi umembala wao; kuonanso malamulo a mpingo pa zokhuza nchito ya utumiki ndi zina.

Maphunziro awa atatha, guru loyesa atumiki ngati ali okwaniritsa zoyenera mtumiki likonzedwa kuti akayese atumiki powafunsa mafunso kuti akacita bwino adzozedwe. Mpingo ungaitane guru loyesali maka-maka m'guruli mumapezeka azibusa ndi atumiki odzozedwa kucokera ku mipingo ya Baptist. Mipingo ina yakhala ili kuitana wacimishoni wothandizira kukula kwa mipingo wa mdela lao kuti aitanitse guru loyesa. Guruli litabvomera kugwira nchitoyi, tsiku liikidwa la kuyesa atumiki.

Pa nthawi ya kuyesa munthu aliyense ayesedwa payekha. Ngati mtumiki woyesedwa ali wokwatira, mkazi wace afunsidwa kupezeka pa kuyesa. Mafunso angafunsidwe kapena sangafunsidwe akukhudza m'mene wina m'cikwati aganizira pa mnzace kukhala mtumiki kapena pa m'mene banja lao liri ndi utumiki wao wa uzimu mu banja lao. Wakumpando wa guru ili la oyesa kawiri-kawiri ndiye yemwe akhala mtsogoleri pa kufunsa mafunso. Mafunso amene amafunsidwa ndi okhudza za cipulumutso ca mtumiki watsopano, nchito za mu mpingo zimene iye anacitanso cangu pa kucita, zimene akhulupirira pa za Mau a Mulungu, ciyanjano cace ndi mbusa, atumiki ena ndi mamembala



Zoona Paulo ananena kuti "atumiki akhale...osamwetsa vinyo...." Ena amayesa kugwiritsa malembowo monga cowathandizira pa kumwa kwao. Pa nthawi ya Paulo vinyo unali cakumwa ca anthu. Madzi ambiri siyanali yabwino kumwa. Kumwa madzi kunali kupanga munthu kudwala kwambiri, motero vinyo unakhala cakumwa. Kumwa mopitirira kunali kuledzeretsa. Malembo awa siyali kubvomereza kumwa, koma ndi cenjezo kwa Akristu kuti asamwe vinyo cifukwa ca zocita zimene umacititsa wina kuti azicite. Mtumiki ndi munthu amene sayenera kudzipereka yekha kumwa cakumwa caukali, kapena munthu wopezeka ali kugulitsa vinyo kutsogolera ena kuti acite zinthu zosayenera. Ngati mtumiki apezeka ali kumwa kapena kugulitsa vinyo ndiye kuti m'coonadi uyu sali mtumiki koma m'dzina lokha.

Mtumiki ndi munthu amene sayenera kukhala wa cisiriro conyansa kapena wa umbombo. "Momwemonso atumiki akhale...osati acisiriro conyansa" (1 Timoteo 3:8). Kukhala ndi cuma si cimo ai kapena konyansa. Paulo anali kuyang'anira momwe timatengera cuma. Colinga ca mtumiki cikhale pa kucita cifuniro ca Mulungu koposa kuzikundikira yekha cuma. Pa nthawi ya Paulo nchito ya atumiki inali ya kugawira zoperekedwa kucokera ku anthu kwa ana amasiye, akazi amasiye, osauka ndi a mndende. Anthu anali kudalira kwambiri pa atumiki okhulupirika ndi odzipereka.

Cikondi ca ndalama ciri maka-maka coopsya pa munthu amene pa udindo wace, anaikidwa kuyang'anira pa cuma ca mpingo, ndipo okhuzidwa ndi nchito ya kuziyang'anira zinthuzo. Kwa munthu wokhumba cuma yesero idzakhala lalikulu, komanso kugwiritsa nchito cuma m'njira ya kuthandizira za iye yekha.

Ili ndi cenjezo leni-leni lotsutsa acisiriro conyansa. Cidzaononga moyo wanu ndi utumiki. Cikondi ca pa ndalama ndi cokhuza mtima. Mtumiki ayenera kukhala ndi cikondi cimodzi cokha mu mtima mwace, cikondi cace Ambuye Yesu Kristu.

Mtumiki ndi munthu amene utumiki wace unayesedwa. "Koma iwonso ayambe ayesedwe" (1 Timoteo 3:10). Iye amene ali mtumiki ndi munthu amene watsimikiza kuti ndi woyenera kutumikira pa udindo wace mu mzimu. Kuyesedwa kwace sikuli komupatsa mphamvu ya kuyankha bwino mafunso ena. Maka-maka, anapambana mayeso mu njira ya Cikristu imene iye anazionetsera yekha mu macitidwe ndi m'malankhulidwe. Waonetsa kukula kwace mu mzimu. Wayesedwa ndi kupezeka

woona mu mbali zonse za moyo wace, osati cifukwa ca maonekedwe ace abwino, cangu cace, m'mene ali ku nchito, kapena kudziwika.

Ufumu wa Mulungu unamangika pa kuyesa. Akristu a ku Roma analamulidwa ndi mtumwi Paulo kuyesa cifuniro ca Mulungu mu miyoyo yao. Mu Agalatiya 6:4 munthu aliyense "ayesere nchito yace ya iye yekha." Yesu anaitana onse amene anamvera iye kuyesa zimene iye (Yesu) ananena mu mtima wace (wa munthu aliyense) ndi zocitika m'moyo akalibe kufika kusankha komaliza. Ngati kuyesa ndi comwe Mulungu anamangirapo ufumu wace, sicingakhale cocepekera pa atsogoleri a mpingo, ndi kopambana atumiki amene ali m'malo mwa utsogoleri wa mu mipingo. Malo opambana ali onse amene Mulungu apatsa munthu aliyense, ayembekeza kuti umoyo wace wa munthuyo uyenera kukhala wopanda cirema, cifukwa ambiri ayang'anira moyo wace.



nzeru kuganizira kuti mpingo ungagwiritse nchito njira imene inali yodziwika bwino ndipo anaigwiritsapo kale nchito.

Monga mpingo wa okhulupirira odzipereka kutsatira zocita okhulupirira mu nthawi ya Cipangano Catsopano, mipingo ya Baptist ikhulupirira kuti kasankhidwe ka atsogoleri a m'mipingo mu njira ya mu Cipangano Catsopano ndi pamene a mpingo onse pamodzi ndiponso payekha-payekha apemphera, asankha oti ayimilire pa masankho ndi kusankha atsogoleri, pamene pakati pao pali atumiki. Motero, kusankha atumiki ndi nchito ya mpingo wonse wa a Baptist okhulupirira; si nchito ya munthu m'modzi kapena anthu ocepekera amene ali mamembala a mpingo ai. Monga a Baptist tiyenera kukhala olimbika mu kutsatira zimene tikhulupirira kuti ndiye njira ya mu Cipangano Catsopano ya kusankhiramo atsogoleri.

Zofuna mpingo ndiye zidzationetsera ndi atumiki angati mpingo uyenera kuti usankhe. Mpingo wa ku Yerusalemu unabvomerezana pa atumiki asanu ndi awiri kuti atenge malo a utsogoleri, amene anali "odzala ndi mzimu ndi anzeru." Cingakhale kuti mpingo lero lino ungagwirizane kukhala ndi atumiki ocepekerapo kapena acurukirapo mu mpingo wao. Angakhale atumiki angati amene mpingo ufuna, mpingo uyenera kutsatira njira imene inagwiritsidwa nchito pa kusankha atumiki asanu ndi awiri a mpingo wa ku Yerusalemu monga: Coyamba, anagwirizana atsogoleri adzakhala angati. Caciwiri, anapemphera, kupempha Mulungu kuti awatsogolere kusankha munthu wofunikira kutenga udindo. Cacitatu, anasankha m'mene adzaimirira pa masankho m'mene Mzimu Woyera anawatsogolera. Cacinai, anasankha pa kucita maere (kuponya mapepala) kusankha ati atenge maudindo a utsogoleri. Kupyolera mu njirazi, mpingo wa ku Yerusalemu unakwaniritsa nchito yao ya kusankha atumiki awo.

## KUSANKHA KWA ATUMIKI

Kusankha mamembala a mpingo amene aonetsa utsogoleri wa uzimu ndi kukula mu mzimu kuti atumikire monga atumiki mu mpingo wa Baptist ndi nchito ya mpingo wonse. Sinchito ya munthu m'modzi kapena mamembala a mpingo ocepekera ai. Iyi ndi nchito yokhuza mamembala onse a mu mpingo.

Mu Macitidwe 6 atumwi analamulira mpingo wa okhulupirira mu Yerusalemu. "Yang'anani mwa inu amuna asanu ndi awiri ambiri yabwino, odzala ndi Mzimu ndi nzeru" (ndime 3). Wolemba apitiriza mu ndime 5, "Ndipo mau amene anakonda unyinji wonse."

Guru la okhulupirira inacita nchito ija ya kusankha amuna amene adzatumikira monga atumiki ace. Ndi utsogoleri wa mzimu woyera anakwaniritsa nchitoyi mogwirizana m'modzi ndi m'modzi. Mogwirizana anacita monga thupi limodzi, m'modzi-m'modzi anathandizira kusankha atumiki.

Wolemba wa Macitidwe sanamasulire njira imene mpingo unagwiritsa nchito pa kusankha amuna asanu ndi awiri. Njira imene anagwiritsa ingakhale monga kubvomereza onse pamodzi ndi mtumiki m'modzi-m'modzi kapena monga guru mogwirizana. Komanso, cionekanso monga kuti mpingo unagwiritsa nchito njira imene anasankhiramo Matiya pa kudzadza malo anasiidwa ndi Yudase Isikariote, uku ndi kupemphera, kusankha woti aimirire pa masankho ndi kusankha pa kuponya mapepala. "Ndipo anaikidwapo awiri, Yosefe wochedwa Barsaba, (amene anachedwanso Yusto) ndi Matiya. Ndipo anapemphera...ndipo anayesa maere pa iwo; ndipo anagwera Matiya..." (Macitidwe 1:23,24,26). Kucokera pomwepo iyi inali njira imene inagwiritsidwa nchito ndi mpingo pa kudzadza malo ya atumwi, cionekanso ca nzeru kuti anagwiritsanso nchito njirayi pa kusankha atumiki asanu ndi awiri kupemphera, kusankha oti asankhidwe ndi kusankha pa kuponya mapepala.

Ngakhale kuti pali "cete mu mzimu" mu njira imene anagwiritsa nchito mu mpingo wa ku Yerusalemu mu kasankhidwe ka asanu ndi awiri, malembo sali cete pa njira ya kasankhidwe imene anaigwiritsa nchito pa kusankha amene anatenga malo ya Yudasi. Motero, mu kasankhidwe ka atumiki asanu ndi awiri, cioneka ca



# GAWO LACIWIRI

## ATUMIKI: KUTUMIKIRA PA KUONETSA CITSANZO

Yesu ndiye citsanzo cimene Akristu ayenera kutsatira mu miyoyo yao. Yesu, ku okhulupirira, amakhala citsanzo ca umoyo wodzala mwa Mulungu. Ndithudi, Yesu ationetsa ife momwe tingakhalire umoyo wokwanira ndi wocuruka ndi wodzala pamene umoyo uperekedwa kwathunthu osasiyako mbali ina ili yonse ku cifuniro ca Mulungu, Atate.

Atsogoleri a mipingo ali ndi utumiki wa kuonetsa zitsanzo kwa Akristu cifukwa ca udindo wao wa utsogoleri mu mpingo. Mbusa ali ndi utumiki wa kukonza khalidwe labwino la anthu ndi umoyo wa uzimu wabwino (mwa citsanzo) ku anthu a Mulungu ndi anthu amene alibe mbali ya ciyanjano ca okhulupirira. Mtumiki ndi mtsogoleri wina amene utumiki wace ukhudza kuonetsa citsanzo.

Nthawi zina kukhala citsanzo mu utumiki wa mtumiki uli ndi mphamvu ku anthu a mu mpingo ndi ku anthu ena otizungulira kuposa mbusa. Abusa kawiri-kawiri amaganiziridwa kukhala a uzimu ndi a cipembedzo kupambana membala wa mpingo cifukwa iye, mbusa, ali ndi maitanidwe a padera ocokera kwa Mulungu. M'njira ina mtumiki ndi mtsogoleri wa mpingo amene umoyo wace wa uzimu umalinganizidwa ku membala wa mpingo. Atumiki amasankhidwa kucokera ku mamembala a mpingo, koma mbusa kawiri-kawiri amacokera ku mpingo wina wosiyana ndi mamembala a mpingo amene atsogolera. Cifukwa ca kulingana kwa mtumiki ndi "anthu okhala mu mipando" mu mpingo, atumiki ali ndi udindo wa padera wokhuza anthu mu utumiki pa kupereka citsanzo. Pali njira zambiri zimene atumiki amakhuzira kwa kukuru mamembala ena a mpingo mu utumiki wao kukhala citsanzo.

Mu mitu yotsatira tidzayang'ana pa zina zimene zimakhudza miyoyo ya anthu zimene mtumiki ali nazo kupyolera mukukhala iye citsanzo.

Mbusa wodzozedwa ngati wamva kuitana kwa Mulungu kuti acoke pa mpingo umene unamudzoza ndi kupita ku mpingo wina kukatumikira monga mbusa, mbusa sadzozedwanso ndi mpingo umene wa muitana kuti akhale mbusa wao. Kudzoza kucokera ku mpingo wina umayesedwa wokwanira.

Kuyang'ana pa kudzoza mu njira iyi ndi m'ciunikiro ca ziphunzitso ca mpingo wa mu Cipangano Catsopano, kudzoza cimakhala cinthu cofunikira ndi catanthauzo ku mpingo umene umadzoza abusa ndi atumiki ao ndi kwa iwo wodzozedwa. Kudzoza kumatsimikiza cifuniro ca Mulungu pa munthu amene adzozedwa ngakhalenso ku mpingo womwe umene udzoza.

Kudzoza uku ndi "kuika kwa manja" sikupatsa munthu mphamvu ya padera kapena kupatsa ukuru wa za uzimu pamaso pa Mulungu. Mu 1 Timoteo 4:14 Paulo alimbikitsa, "Usanyalapse mphatsoyo ili mwa iwe, yopatsidwa kwa iwe mwa cinenero, pamodzi ndi kuika kwa manja a akuru."

Guru loyesa ili ngati guru imene inaika Timoteo padera kuti acite nchito yomwe Mulungu anamuitanira. Kuika padera kolingana kuoneka pa kusankha asanu ndi awiri (Macitidwe 6:1-6) ndi pa kutumiza kwa Paulo ndi Barnaba ndi mpingo ku Antiokeya (Macitidwe 13:1-3).

Mphatso ya uzimu imene Paulo alankhulapo ndi ija imene Timoteo anapatsidwa ndi Ambuye. Mphatso siinapatsidwa ndi guru la akulu ai. Kapena simwambo wa kuika manja umene unapereka mphatso ya uzimu ya kucita nchito.

Pa nthawi ya Cipangano Catsopano, anthu anali kudzozedwa pa nchito ya padera ndi mpingo wa okhulupirira. Asanu ndi awiri mu Macitidwe 6 anasankhidwa kuti atumikire pa zofunikira ku amasiye a Cikristu a Cihelene amene anali kuiwalika pa citumikiro ca tsiku ndi tsiku. Asanu awa ndi awiri ndiye anali atumiki oyamba mu mbiri ya utumiki.

Paulo ndi Barnaba "anadzozedwa" pa kuikidwa manja mu mpingo mu Antiokeya akalibe kupita pa ulendo wao wa kukagwira nchito.

Kudzoza kwa abusa ndi atumiki mu mipingo ya Baptist lero ili yoyenera ndi yofunikira kwambiri monga momwe cinaliri mu nthawi ya Cipangano Catsopano. Mwambo wace ukali ndithu wofunikira ndi wa cikumbutso mu mpingo cimodzi-modzinso ku omwe ali kudzozedwa. Kudzoza kwa abusa kapena atumiki cimakhala cibvomerezo ku mipingo ina ya Baptist. Komanso, tiyenera kukumbukira kuti kudzoza sikupatsa wodzozedwayo mphamvu ya padera pa ena onse.

Mtumiki wodzozedwa akapita kukakhala kwina sapita kukakhala mtumiki ku mpingo wa Baptist wina cifukwa anadzozedwa kale ku mpingo wina wa Baptist.

Mpingo wa Baptist kumene mtumiki wamukako, pambuyo pa kuyang'anira ndi kuona khalidwe la utumiki wace, ungamupemphe kuti atumikire monga m'modzi wa atumiki. Kambiri-mbiri, mpingo ungabvomereze kudzozedwa kwace kucokera ku mpingo wina wa Baptist ndipo mpingo sungaitanitse msonkhano wina wakuti adzoze mtumikiyo.





## MTUMIKI KUTUMIKIRA PAKUKHALA CITSANZO MUKAPHUNZITSIDWE KAKUKULA MU UZIMU

Mbusa anali kulankhula kwa atumiki a mu mpingo. Zokambirana zinafika pa kufunikira kwa kupezeka ku zocitika (maprogramu) mu mpingo zolinga kukula mu mzimu. M'modzi wa atumiki, mu maganizo ace pakusowa mtendere cifukwa ca kusapezeka ku Sande Sukulu, anati, "Pamene ndinali wa kumpando wa atumiki, abusa, ndinali kupezeka ku Sande Sukulu." Abusa anamuyankha, "Inde, munali kupezeka caka cija." Pa nthawi imene iwo anali a kumpando wa atumiki, mtumiki uja anaona kufunikira kwa kupezeka ndi kutengako mbali mu (maprogramu) m'ndandanda wolinga pa za kukula mu mzimu. Anasiya kupezeka pamene anasiya kukhala wa kumpando wa atumiki. Kodi ndiye kuti tsopano sanali kufunikira za kukula mu mzimu cifukwa sanali wa kumpando wa atumiki?

Ngakhale kuti mtumiki uja sanalinso wa kumpando koma anali akali kutumikira monga mtumiki mu mpingo. Malo ace a utsogoleri monga mtumiki anali cimodzi-modzi. Koma kuti mphamvu za utsogoleri pakati pa atumiki anzao zinacepekerako. Udindo wao wa kuphunzitsa kukula mu uzimu pakukhala citsanzo unalipo monga pa nthawi imene anali wa kumpando wa atumiki.

Mu buku, *Mtumiki wa Baptist,* wolemba Dr. Robert E. Naylor ananena kuti cingakhale cinthu codabwitsa kwambiri pakati pa mamembala a mpingo ngati atumiki onse a mpingo atayamba kupezeka ku maprogramu yonse ya mpingo ya kukhuza zakukula mu uzimu. Dr. Naylor anapitiriza kunena kuti ngati zinayenera kucitika mtumiki aliyense "adzapeza kuti wakoka anthu ena ambiri kuti aone udindo wao mu kuphunzitsa mamembala a mpingo" (*Mtumiki wa Baptist,* yolembedwa ndi a Robert E. Naylor, samba 99).

Atumiki ayenera kuzindikira kuti citsanzo cao mu maphunziro a kukula mu mzimu angakhale nthawi zina obvomerezeka kapena otsutsa. Ngati kuphunzitsa kukula mu mzimu kuli kofunikira kwa mtumiki kotero kuti ayamba kupezeka kuzocitika, pomwepo ena adzatsatira citsanzo pa kulembetsa dzina ndi kuyamba kupezeka ku maphunziro a kukula mu uzimu. Zotsutsanso ziri zoona. Ngati mtumiki alephera kupezeka ku maphunziro a kukula mu uzimu

ku mpingo wace, pomwepo ena sadzaona kufunikira kwace kwa maphunzirowo. Iwo ali kutsatira cabe mtsogoleri, amene ali mtumiki.

Mu mndandanda wa maphunziro a kukula mu mzimu mu mpingo palibe munthu wina amene anthu amayang'anirako citsanzo kuposa mtumiki. Atumiki amasankhidwa ku utumiki cifukwa ca kukula mu uzimu ndi mu kuphunzitsa. Ngati atsogoleri a mpingo aonetsa kufunikira kwace kwa kuonjezapo maphunziro akukula mu mzimu, ici cimakhala citsanzo ku mamembala ena a mpingo kuti naonso afunikira maphunziro a kukula mu mzimu pa mpingo kumacititsa kuti mamembala ambiri a mpingo aleke kumapezeka ku maphunziro. Kuthandizira maphunziro ya kukula mu mzimu ndi umboni kapena cibvomerezeka ndi atumiki pamene iwo apezekako monga wophunzira. Kopanda kupezeka kulibe kuthandizira. Mamembala ndi anthu wamba afuna kuona "kuyenda" kwa mtumiki kulingana ndi "kalankhulidwe" kace.

Dr. Naylor anapitiriza kunena pa atumiki kuti, "Maina oyamba kulembedwa pa zonse mu mpingo...ayenera kukhala ya atumiki. Guru loyamba kupezeka pa la Mulungu...ayenera kukhala atumiki. Munthu woyamba kupezeka pa malo ace a maphunziro (a mulungu ndi mulungu) ayenera kukhala mtumiki. Cimodzi-modzi, ngakhale maphunziro a m'manyumba kapena kuti mpata wa maphunziro ku asosiyeshoni apezeka, mtumiki ayenera kukhala munthu woyamba kupezeka." (p.98)

Kulembetsa cabe dzina ndi kupezeka ku mndandanda wa za kukula mu mzimu pa mpingo pace sicitanthauza kuti ndizokhazo zimene mtumiki ayenera kucita pa zocitika pa mndandandawu. Pakuthandizira mndandanda kwathunthu mtumiki adzayenera (1) kutukula mpata uli onse wa zakukula mwa uzimu mu mpingo. (2) Adzalimbikitsa ena molimba kutengako mbali pa mpata wa za kukula mu mzimu. (3) Adzakhala mtsogoleri pa zocitika pamene aitanidwa kuti aphunzitse kapena kuti akhale mkonzi. (4) Adzagwiritsa nchito zonse zimene adzaphunzira pa maphunziro onse amene adzalandira kotero kuti ena apeze kukula mwa mzimu kupyolera mu utsogoleri wace. "Pamene munthu asankhidwa kukhala mtumiki, alibenso sankho yakuti 'kapena' iye adzaonetsa citsanzo mu maphunziro. Sankho yace imene angapange ndi yakuti ndi citsanzo cotani cimene adzapatsa." (Sam Brents, *Mtumiki Opatsa Citsanzo.*)





## KUDZOZA: ZIKHULUPIRIRO NDI ZA KUCITA A BAPTIST

Kusamvetsetsa pa zikhulupiriro ndi miyambo ina ya a Baptist ndi zodziwika kwambiri ku mamembala ena a mpingo ya Baptist. Kudzoza ndi mbali imodzi imene zikhulupiriro ndi mwambo wa a Baptist nthawi zina saumvetsetsa. Abusa ndi atumiki ndi maofisala okhawo awiri amene anadzozedwa mu mpingo woyamba monga timapezera mu buku la Macitidwe ndi m'makalata a mtumwi Paulo.

Pali zokambidwa zisanu zimene zimasulira za a Baptist kapena zimene amakhulupirira pa za kudzoza kwa mbusa ndi atumiki.

Coyamba, kudzoza ndi citsimikizo capoyera ca mpingo kuti ukhulupirira kuti munthu anapatsidwa ndi Mzimu Woyera kutumikira pa nchito ya ubusa kapena utumiki.

Caciwiri, ndi mpingo kupatsa mphamvu ku munthu kuti acite nchito ya kuthandiza imene Mzimu Woyera unampatsa.

Cacitatu, ndi nthawi ya kupempherera munthuyo mu nchito yace ndi kulonjeza kupempherera mu nchito yace.

Cacinai, kudzoza kwa mbusa kapena atumiki ndi nchito ya mpingo kapena mipingo kugwirizana pamodzi.

Cacisanu, pamene kudzoza kutsimikiza mphatso za uzimu ku munthu ya kugwira nchito ndi kumpatulira kucita nchito ya padera. Kudzoza kulibe phindu kapena mphamvu kupambana mpingo umene uitana kudzoza munthu.

Monga mwambiri ya Baptist ndi mwambo, akana ciphunzitso ca kuti kudzoza kukweza munthu wodzozedwa kukhala munthu woyera. A Baptist sakhulupirira kuti wodzozedwayo ali wa uzimu kwambiri kuposa amene ali wosadzozedwa.

A Baptist amakana ciphunzitso ca kuti kudzoza kutanthauza kuti yekhayo wodzozedwa angafike kwa Mulungu ndi kutsogolera pa zocitika ziwiri za mu mpingo, Mgonero wa Ambuye ndi ubatizo.

A Baptist akhulupirira kuti anthu onse ali ansembe pamaso a Mulungu ndipo angafike kwa Mulungu osapitira mwa odzozedwa. A Baptist akhulupiriranso kuti mpingo ungabvomereze membala aliyense kuti abatize okhulupirira atsopano ndi kupereka Mgonero wa Ambuye. Cipangano Catsopano cimationetsera ici pa kudzoza ndi zocitika mu mpingo.

## MTUMIKI ATHANDIZIRA PA KUPATSA CITSANZO CAKHALIDWE LA MOYO WACE

Kodi mpingo umene wadzoza mtumiki umayembekezera zambiri kucokera ku mtumikiyo mu kudzipereka yekha koposa momwe uyembekezera membala wina aliyense mu mpingo? Mtumwi Paulo apatsa yankho yabwino kwambiri kufunso mu kalata yace yoyamba ku mwana wace wa uzimu, Timoteo. Paulo analemba kwa Timoteo, "Khala citsanzo kwa iwo okhulupira" (1 Timoteo 4:12). Palibe angakane kuti mauwa akhudza Akristu onse, koma maka-maka alimbikitsa kufunikira kwa atumiki kukhala citsanzo ca padera. Anthu amisinkhu yonse ayang'anire pa umoyo umene uli ngati citsanzo cimene angatsatire. Mu mpingo wa Baptist mtumiki ndi munthu woyamba yemwe anthu onse a mu mpingo amayang'anira kukhala citsanzo mu umoyo wa Cikristu, uku ndikuti, m'njira imene Mkristu amakhalira tsiku ndi tsiku.

Mtumiki amene amakhala citsanzo pa kutsatira khalidwe la Cikristu kuonetsa m'mene umoyo wa Cikristu weni-weni uliri. Aonetsanso kuti iwo anamusankha iye kukhala mtumiki sanalakwe mu kusankha kwao kuti iye atumikire mu utumiki wa mu mpingo.

Paulo, pa kulembera Timoteo, anapatsa mndandanda wa mbali imene citsanzo cingaperekedwe ku anthu. Mbali zace ndi izi: "Mu malakhulidwe ndi mu zicitidwe, mu cikondi, mu cikhulupiriro ndi mu ciyeso." Mbali zonsezi zikhudza umoyo wa munthu aliyense payekha-payekha.

*"Mu kalankhulidwe"*

Mau amene munthu amalankhula ndi mkamwa mwace amaonetsa zimene ziri mkati mwa munthu. Mau kapena kalankhulidwe kace mtumiki mu zocitika tsiku ndi tsiku zimaonetsa kuti ali munthu wotani mu mtima wace wa mtumiki uyu. Mtumiki angakondwere mu zinthu zambiri zimene ziri zabwino koma osatengako mbali mu nkhani zoipa ndi zopanda pace, uku ndi kuti, zoopsya ndi za ucimo.

Mtumiki ayenera kukhala ndi malankhulidwe abwino, kugwiritsa nchito mau amene ali a ulemu, oyera ndi opanda cimo. Kalankhulidwe kace kakhala monga adziwira kuti Ambuye Yesu Kristu angagwiritse nchito pa nthawiyo, pa zocitika ndi pa malo. Malankhulidwe a mtumiki amene asewenzetsa mu zocitika tsiku

liri lonse, nthawi ili yonse akhale monga mpimo umene anthu adzapimirapo kuimirira kwace monga mtumiki.

*"Kacitidwe"*

Mtumiki mu zicitidwe zace ayenera kuti akhale wopanda cirema. Anthu a mu mpingo maka-maka anthu amene akhala kumene mtumiki akhala ndi ku malo kumene agwira nchito nthawi zonse amayang'anira njira imene mtumiki amacitira. Mafunso amene anthu afunsa pa za mtumiki mozindikira kapena mosazindikira pa za mtumiki ndi awa: Kodi mtumiki amagwira bwino nchito kumene amasewenza? Kodi mtumiki ali okhulupirika pa kabweredwe ku nthawi ya nchito? Kodi mtumiki amene ali wa malonda amagwiritsa nchito njira za Cikristu kuomugula ndi anchito? Kodi anchito ace amagwiritsa nchito njira ya Cikristu? Kodi mtumikiyo amasankha zinthu zosoweretsa ndi masowera amene ali abwino ku umoyo ndi khalidwe la umunthu imene ili yobvomerezeka ku Mkristu? Kodi mtumiki amasunga banja lace mwa ulemu ndi molemekezeka? (Ulemu ndi kulemekeza citanthauza kuposa kuwapatsa nyumba, zakudya ndi zobvala. Ici citanthauza kuyang'ana pa membala aliyense wa pa banja kuti ali kupatsidwa ulemu monga munthu.)

*"Mu cikhulupiriro"*

Umoyo wa mtumiki umaonetsa coonadi ca cikhulupiriro cace. Kuonetsa kuti akhala kapena sakhala mwa cikhulupiriro zimaonekera ku umoyo wace. Ngati wina sakhala "mu cikhulupiriro" mu umoyo wace wa uzimu, ndiye kuti palibe njira imene iye angakhaliremo citsanzo ca kukhala mu cipulumutso ku ena amene amakumana naye. Mtumiki ayenera kukhala umoyo wa kukhulupirira kuti Mulungu ali pa ulamuliro pa moyo, ndi pa zocitika. Mtumiki amaonetsa cikhulupiriro cace pa kulankhula ndi Mulungu kawiri-kawiri mwa pemphero. Pamene nthawi za mabvuto zimufikira iye, mtumiki adzakhoza kuimirira pa nthawi za mabvuto cifukwa ca cikhulupiriro coona mwa Mulungu ndi mu cidziwitso cace kuti Mulungu agwira nchito zonse kucitira ubwino. Cikhulupiriro coonaci kumbali ya mtumiki ciri kubvomereza kotheratu ndi wolemba nyimbo amene analemba "Khala ndi cikhulupiriro mwa Mulungu, ali pa mpando wace wa cifumu; Khala ndi cikhulupiriro mwa Mulungu, amayang'anira ace; Iye salephera, ayenera kupambana, Khala ndi cikhulupiriro mwa Mulungu, khala ndi cikhulupiriro mwa Mulungu."



# GAWO LACITATU

## KUSANKHA NDI KUDZOZA KWA ATUMIKI

Mpingo uyenera kusankha ndi kudzoza atumiki ace motsimikiza ndi maganizo akutsogozedwa ndi Mulungu.

Kusankha kwa atumiki ndi kupempha mpingo kuti ucite cinthu cina cimene ciri ca ciwiri cofunikira ku utsogoleri wa mbusa. Ndi nchito ya utsogoleri mu mpingo ndi zocitika pa za kuthandizira pa za uzimu.

Kudzoza ndi kubvomereza kwa mpingo motsimikiza pa cikonzero ca mapemphero awo amene anasankhidwa kukhala atumiki kuti acite mwa kukula mu uzimu kukwaniritsa nchito yao ya utsogoleri mu mpingo. Ndi kubvomerezanso kwa atumiki pa msonkhano wa anthu ambiri kudzipereka kwao kuti adzakwaniritsa nchito ya utumiki. Kudzoza ndi kupereka utumiki ku anthu a Mulungu mu mpingo ndi ku anthu amene sadziwa Mulungu monga Tate amene ali kunja kwa mpingo. Ndi mpingo kubvomereza nchito yace ya ukapolo ndi atumiki kubvomereza nchito ya ukapolo mu miyoyo yao.

za phindu zokhuza mpingo, koma ayeneranso kukhala okonzeka kumvera ku maganizo ena. Zakukonza ndi zofunikira za anthu mu mpingo ziyenera kukhala zoyamba kukonza.

Atumiki ali ngati gulu ngakhale kuti ali munthu payekha-payekha pa nchito imene adzacita pa okha. Kugwirira nchito pamodzi monga guru ndi citsanzo ca kukula mu uzimu kwa mpingo. Kugwirizana pakati pa atumiki cidzapatsa citsanzo pamaso pa maguru ena mu mpingo ndipo cidzathandizira cigwirizano mu maguru ena awa. Mtumiki amene safuna cocitika cina mu mpingo adzafoketsa mphamvu ya guru ya atumiki kukweza mndandanda wonse wa utumiki mu mpingo.

**POTSILIZA:**

Mpingo mu Cipangano Catsopano mu macitidwe unakula mu nambala ndi mu mzimu cifukwa ca cigwirizano cimene cinapezeka pakati pa anthu a mu mpingo. Mpingo wa masiku ano ufunsidwa kuti ukhale wolimba ndi kugwirizana mwa Kristu pamene ukumana ndi zambiri zofunikira kuti uzicite. Atumiki a mipingo a masiku ano akumana ndi nchito ya kutumikira pa kukhala zitsanzo. Anthu ayang'ana pa atumiki a mu mpingo. Zocita atumiki, zabwino kapena zoipa, zidzakhala zodziwika ndipo zidzakumbukidwa nthawi zonse. Cikondi ceni-ceni ca pa Yesu ndi mpingo wace zidzakhala maziko a mtumiki mu nchito yace imene itsogozedwa patsogolo pa kukhala citsanzo.



*"Mciyero"*

Umoyo wa mtumiki uyenera nthawizonse kukhala wopanda cirema. Ngati umoyo wa mtumiki siuli wotero, palibe njira imene iye angakhalire woyenera kukhala citsanzo pakati pa anthu a mu mpingo wace kapena omuzungulira. Colinga ceni-ceni cakuyera cipezeka m'mau a mu nyimbo, "Khala woyera ndi wangwiro mkati, ena aone Yesu mwa iwe." Kulibe malo mu utumiki wa mu mpingo kuti mtumiki aziyanjana ndi cimo. Ngati mtumiki akhala mosayenera, mtumikiyo ayenera kuti acotsedwe pa utumiki lomwelo ndi mpingo uneneretu kuti wacotsa ngakhale kudzozedwa kwa utumiki. Mpingo umene unadzoza mtumiki ulinso ndi mphamvu ndi ulamuliro wocotsa kudzozedwako. Kukhala umoyo wa ucimo ndiye cocititsa kuti kudzozedwa kucotsedwe.

## MTUMIKI ATUMIKIRA PA KUKHALA CITSANZO PA KHALIDWE LA BANJA LACE

Nyumba ya mtumiki ndi cinthu cacikulu. Mu 1 Timoteo 3 ndi comveka bwino kucokera kuzofunikira atumiki zopatsidwa ndi Paulo kuti banja la mtumiki likhale citsanzo cabwino. Ici cikhudza umoyo wa nyumba ya munthu amene anabvomerezedwa kutumikira monga mtumiki, ndi citsanzo cabwino ca pa nyumba ciyenera kupitirizabe ngakhale munthu atadzozedwa monga mtumiki. Kodi ndi m'njira yotani nyumba ya mtumiki ingakhalire citsanzo?

Njira imodzi ndi yakuti mtumiki ayenera kubvomereza udindo wace ndi kuyamba mapemphero ya pa banja lace m'nyumba yace. Mtumiki, podziwa kuti Mulungu adzalemekezedwa ndi cipembedzo m'nyumba yace ndiponso ku mpingo, adzatsogolera mu mapemphero a nthawi ndi nthawi m'nyumba. Ngati alibe zomuthandizira pa mapemphero ya pa banja, mtumiki angawerenge ndime kucokera mu Buku Lopatulika ku banja lace ndi kutsogolera banja mu nthawi ya mapemphero.

Nthawi ya mapemphero a pa banja adzadalira pa zocitika. Mabanja afunika mapemphero ogwirizana ndiponso mapemphero a pa banja. Mabanja ena adzapeza kuti nthawi ya m'mawa ndiye nthawi yabwino kwa iwo pamene ena adzapeza kuti m'madzulo ndiye nthawi zabwino ku banja lao.

Mtumiki atsogolera banja lace mu kupembedza ndi kutumikira mu mpingo. Mabanja akufunika cigwirizano ndi kukhalanso ndi mapemphero a pa banja. Banja la atumiki limapatulidwa pa zofunikirazi. Kuonjezapo mapemphero a pa banja ndi utumiki wa pa zocitika pa mapemphero a ku mpingo ndi utumiki uwu udzabweretsa mugwirizano umene uli wobvuta mu mabanja ena m'njira ina ili yonse. Cidzabweretsa mugwirizano wa mzimu womangiriridwa ndi cisomo ca Mulungu mu banja. Pa kuikamo banja lace, maka-maka ana mu cigwirizano ca mapemphero ndi utumiki, mtumiki aphunzitsa banja lace kuti mapemphero ndi utumiki mu mpingo ndi cinthu cofunikira kwambiri ndi coyenera pa kukula kwao mu mzimu. Ici cidzathandiza ana kubvomereza zinthu zofunikira za uzimu pa iwo wokha kupambana iwo kungobvomereza cabe ndi kutsatira zotsatira za uzimu za makolo ao.





## MTUMIKI AMATUMIKIRA PA KUKHALA CITSANZO PA KUTHANDIZIRA MBUSA NDI ZOCITIKA ZA UZIMU KUTHANDIZIRA PA MPINGO

Mwambo wa kudzoza atumiki umaonetsa cinthu cina ca padera ku munthu cosiyana ndi cinthu cina cocitika mu umoyo cimene cinamuonekera. Mwamboyu ndi wa pafupi, catanthauzo ndi cosaiwalika. Pamene zonse zocitika pa mwambo wa kudzoza zatha, mtumiki apita ndi kukhala citsanzo ca utsogoleri wa Cikristu pa kuthandizira mbusa wace ndi zocitika za uzimu zothandizira pa mpingo.

Nchito za mbusa ndi zambiri. Mwatsoka zofunikira kuti mbusa acite zocuruka, kwakuti abusa ambiri alibe nthawi zokwanira ya kuti akonzekere mokwanira pa za ulaliki a Mau a Mulungu ku mpingo pa tsiku la Mulungu. Pakufuna kukwaniritsa zonse zimene zinaikidwa pa iye kuti zicitike ndi iye, mbusa akhala ndi zambiri zakuti acite mu thupi ndi m'maganizo. Mtumiki angathandizire pa kucepetsanso zina zocita mbusa. Njira ziwiri za kuthandizira ndi kukumana ndi bungwe (komiti) ndikuyendela odwala m'malo mwa mbusa. Uku sikuti mbusa ayenera kuleka kuyendela odwala ai, kukumana ndi bungwe ndi kucita, zinthu zina, zimene iye, mbusa, ayenera kuti acite. Uku ndikuti pakucita zina za izi nthawi ndi nthawi m'malo mwa mbusa, mtumiki adzapatsa mpata kwa mbusa wace wa kupemphera ndi kudzipereka kuwerenga Mau a Mulungu pamene akonzekera kulankhula uthenga wa Mulungu ku anthu m'mawa pa la Mulungu. Kodi ici sindiye cifukwa cimene aja asanu ndi awiri anawasankhila mu Macitidwe 6? Kodi atumiki a masiku ano sayenera kuthandiza mbusa wao m'njira yolingana?

Mtumiki adzapatsanso citsanzo cakuthandiza mbusa pa kumupempherera kawiri-kawiri mosalekeza. Mbusa amamvera ku masuka kwa padera mu mzimu pamene adziwa kuti atumiki ace amupempherera kosaleka. Atumiki amene amapempherera zofuna mbusa wao pa za umoyo wace wa thupi, maganizo ndi mzimu adzafunanso njira zakuti athandizirepo pa zinthu izi. Mtumiki amapatsanso citsanzo cofunikira ca kumvera ndi kuthandizira mwa mphamvu zocitika za kuthandizira za uzimu pa mpingo. Mpingo wa Baptist ndi wa ufulu mu cikonzero cace. Atumiki ali ngati cida mu kupanga colinga, zofunikira ndi malamulo a mu mpingo. Ayenera kukambilana zinthu zimene ziri

Malemba ena amene angagwiritsidwe nchito kucitira umboni ndi awa: Yohane 20:31; 1 Timoteo 1:15; Yohane 3:15-21; Aroma 6:23; Yohane 1:12; Macitidwe 4:19; Macitidwe 16:30, 31; Aefeso 2:4,5; 8-10; 2 Akorinto 6:1-2; Aroma 1:16-17. Malemba awa angagwiritsidwe nchito motsatira mndandanda monga momwe wopelekedwera pa colinga ca cipulumutso pa kucitira umboni ku wosakhulupirira. Kuli malembo ena amene angagwiritsidwe nchito kugawira cikhulupiriro ca wina aliyense mwa Yesu Kristu.

Mtumiki aliyense asakhale wokhutiritsidwa ndi cinthu ciri conse cocepekera pa kukhala wopata miyoyo yotaika wolimba monga momwe angakhalire cifukwa ca Kristu, Ambuye. Pakupatsa citsanzo cotere pamaso pa mamembala ena a mu mpingo, mtumiki adzakhala cilimbikitso ku mamembala ena a mu mpingo kuti akhale wopata miyoyo yotaika kwa Yesu.



Mtumiki azindikira kuti khalidwe limene ana ace aona pa nyumba likhudza m'mene iwo adzakhalira umoyo wao atakula ndi kukhala ndi mabanja awo. Kukhazikika kwa ukwati wa mtumiki umapatsa maziko abwino ku ana ace kuti naonso akakhale ndi zikwati zokhazikika kutsogolo. Ana ocokera ku mabanja a Cikristu amamanga mabanja a Cikristu.

Kufunikira kwa banja la Cikristu mu nyumba ya mtumiki ciyenera kulimbikitsidwa. Atumiki ayenera kukonda akazi awo monga Kristu anakonda mpingo ndi kuzipereka yekha cifukwa ca iwo. Atumiki alimbikitse ndi ndikulangiza ana awo mwa Ambuye Yesu Kristu. Pa kucita izi ndi zina pansi pa ulamuliro wa Yesu Kristu, mtumiki akhale citsanzo ca padera ca banja la Cikristu.

## MTUMIKI ATHANDIZIRA PAKUKHALA ACITSANZO MU DZIKO LA MALONDA

Mtumiki amene ali wamalonda ali ndi mpata wa padera wa kucitira umboni weni-weni wa cipulumutso cace mwa Yesu Kristu. Dziko la malonda ndilodzala ndi anthu amene ayesesa kupeza cuma coculuka. Amagwiritsa nchito anthu monga zitsulo munjira zonse poziunjikira okha cuma cambiri. Anthu awa amene ali ndi njala ya cuma alibe cifundo ca aliyense amene angabvutike cifukwa ca mitengo yonyenga, zinthu zosapangidwa bwino, kugwiritsa nchito anthu anchito mosagwirizana ndi malamulo ogwiriramo nchito.

Mtumiki amene ali wa malonda amadzipeza yekha mu malo a umoyo kumene umboni wa Cikristu nthawi zambiri sutheka kapena sunenedwa. Mtumiki amene ali wa malonda amene analandira cipulumutso mwa Yesu Kristu amadziwa colinga comwe Mulungu amaika pa anthu ndipo adziwe njira zabwino ndi m'mene ayenera kuyendetsera malonda ace. Adziwanso zimene ziri zoyenera ndi cilungamo mukasungidwe ka anthu amene amamugwirira nchito mu malonda ace. Mtumiki amene ali wa malonda ayenera kukhala wolinganiza bwino ndi kulondola cilungamo mu kaikidwe ka mitengo mu malonda ace ndiponso ayenera kuwasewenzetsa anchito ace ndi cilungamo, mwa ulemu ndi cikondi. Ngati alephera kucita zinthu izi, ndiye kuti zonse za Cikristu cace ndi za cabe. Mtumiki amene ali wamalonda ayenera kubvomereza Yesu Kristu kukhala mwini wace weni-weni wa malonda ace ndi kuti iye ali mdindo. Ngati izi ziri tero, pomwepo sipadzakhala mpata wa cisalungamo ciri conse ndi kudzudzula kosayenera kudza kwa iye.

Mtumiki amene ali wa malonda angakhale ndipo ayenera kukhala wosiyana mukacitidwe ka malonda ace kucoka ku wa malonda amene ali wosalinganiza bwino mtengo ndi wosalungama mukacitidwe kace ka malonda. Dziko la malonda ifunitsitsa umboni wa Yesu Kristu. Kodi ali pa malo abwino ndani akupereka umboni ku amalonda ndi ogula kuposa mtumiki amene ali wa malonda? Pa kugwiritsa njira ya Cikristu mu njira zonse za malonda mtumiki ali ndi citsimikizo ca malonjezo apezeka mu Akolose 3:24, "Podziwa kuti mudzalandira kwa Ambuye mphoto ya colowa; Mtumikira Ambuye Kristu mwa ukapolo."





## MTUMIKI ATUMIKIRA PA KUKHALA CITSANZO MUKUCITIRA UMBONI

Kuti atumiki ayenera kudzipereka okha kukucitira umboni kuonetsedwa bwino mu umoyo wa mtumiki, Filipo. "Ndipo Filipo anamuthamangira (mdindo wa ku Atiopiya)...nayamba palembo (Yesaya 53:7,8) nalalikira kwa Iye Yesu" (Macitidwe 8:30,35). Mtumiki, Filipo, anatsogolera mdindo wa ku Antiopiya ku cikhulupiriro ca cipulumutso mwa Yesu Kristu.

Cidzakhala cokumbukirika kuti Filipo anali m'modzi wa amuna asanu ndi awiri anasankhidwa ndi mpingo wa ku Yerusalemu kuti atumikire pa za uzimu mu mpingo. Iye, pamodzi ndi anzace ena asanu ndi m'modzi, anaikidwa padera cifukwa ca nchitoyi ndi atumwi monga akapolo a Ambuye mu mpingo.

Filipo anali wokhulupiririka, wodzala ndi Mzimu Woyera ndi wa nzeru pa kupanga sankho. Mosakaikira analinso wa cifundo kwa ena, anaonetsa poyera cikhulupiriro cace mwa Yesu, anali ndi cangu pa cikhulupiriro cace mwa Yesu, ndipo anali woonadi. Anadziwadi Yesu Kristu, anthu ndi Mau a Mulungu; ndipo anali wokonzeka nthawi zonse kugawira umboni ndi cikhulupiriro ca Mbuye wace kwa ena.

Citsanzo ca Filipo monga mtumiki cikhudza aliyense pa yekha kupata miyoyo yotaika ndipo ici cakhala cofunikira nthawi zonse kwa atumiki kutsatira. Citsanzo cace ndi umboni wakuti atumiki akhale citsanzo ku mamembala ena kuti apedzekenso kucitira umboni. Mtumiki asakhale wokhutira cabe ndi kuthandizira kucitira umboni ndi mau apa kamwa pace pokha ai. Kukhutira kwace mu kupezeka kwace pa nchitoyi ya kucitira umboni, uku ndi kucitira umboni za m'mene adziwira Yesu Kristu ndi Mau a Mulungu ku anthu. Angakhale kuti sicofunikira kwambiri kuti aliyense wasankhidwa kukhala mtumiki ayenera kukhala wopata miyoyo ya anthu kwa Yesu, koma cinthu cimodzi ca padera ndi cakuti akhale ndi mbiri yabwino pakati ka mamembala a mu mpingo monga m'modzi amene nthawi zonse mosalekeza anauzanso osakhulupirira za cikhulupiriro cace mwa Yesu Kristu. Pakugawira cikhulupiriro cace, mtumiki adzagwiritsa nchito Mau a Mulungu pa kuonetsa wosakhulupirira pamene iye waimilira (wosakhulupirira pamaso pa Mulungu) ndi m'mene angayanjanitsidwire ndi Mulungu Atate mwa Yesu Kristu.

## ATUMIKI ATUMIKIRA PA KUKHALA CITSANZO PA KUYENDERA MAMEMBALA ATSOPANO MU MIPINGO

Mu mpingo yonse mbali ya mapemphero ya m'mawa pa la Mulungu ndi kulandira alendo ku mapemphero. Alendo auzidwa m'mene alandiridwira ku mapemphero. Ena amabweranso ndi kukhala a membala a mpingo. Pomwepo, nthawi zina, cibwenzi ndi kalandiridwe kadzidzira.

Cinthu cofunikira cacikulu mu mpingo ndi kuthandizira mamembala atsopano aone kuti ali mbali ya banja ya mpingo. Atumiki angakhale ndi utumiki wa mphamvu mu mbali ya mamembala atsopano kuti akhale mbali ya banja ya mpingo. Atumiki angathandizire mu utumiki wa uzimu pa kutenganso mbali ya kuyendela mamembala atsopano. Pakutenganso mbali ya mndandanda wa kuyendelaku, atumiki ali kukwaniritsa zofunikira mu Cipangano Catsopano, kuthandizira mbusa, kudzilimbikitsa okha mu utumiki ndi kulimbikitsa banja la mpingo. Pakuonjezanso kuyendela kwace kwa mamembala atsopano ndi kuyendela kwa mbusa ndi mamembala ena, ndiye kuti mtumiki ali kupatsa citsanzo cabwino ca Cikristu ca kusamalira ndi kuganizira za anthu.

Pakuti mtumiki ndi Mkristu wokula, adzakhoza kuthandizira zofunikira ku membala watsopano. Angayankhe mafunso pa zokhulupirira a Baptist, zimene amacita ndi ciphunzitso cao, mndandanda wa m'mene amagwirira nchito ndi mpata wa utumiki wa mamembala atsopano pa zocitika mu mpingo. Angauze membala watsopano m'mene angapezere mphindu pa kutenganso mbali molimbika kwathunthu ku zocitika zonse za mu mpingo kupanga membala watsopano kukhala womasuka kwathunthu mu mpingo wace watsopano kuli kofunikira ndithu. Mtumiki ayenera kuthandizira membala watsopano kuti akhale ali kuona kuti zoona ali ndi mpingo wace ndikuti iye ali ciwalo cofunikira ca banja la mpingo.

"Mtumiki kuyendela mamembala atsopano kulondola citsanzo ca mu Buku Lopatulika. Cikwaniritsa utumiki wa uzimu. Cithandizira mbusa. Cilimbikitsa atumiki. Cipanga nthawi zina mpingo wodzidzira kuoneka monga wofunda ndi ciyanjano ceni-ceni ca Cikristu."





## MTUMIKI ATHANDIZIRA PA KUKHALA CITSANZO KU MALO KUMENE AGWIRA NCHITO

Mtumwi Paulo anaika zofunikira mu Akolose 3:22-25 cimene cikhudza Mkristu amene analowetsedwa nchito. Ngakhale kuti ndimeyi siilankhula motsimikiza kwa atumiki, ilankhula kwa iwo mu nchito yao. Paulo analimbikitsa Akristu kugwira nchito kumalo komwe agwira nchito monga agwirira nchito Ambuye Yesu Kristu m'malo mwa owalemba nchito.

Mtumiki amene ali wolembedwa nchito ali ndi mpata osati wocitira umboni wokha wa cikhulupiriro cace pa nchito koma kukhala citsanzo ku anchito anzace pamene ali kugwira nchito yace monga Mkristu. Ici citanthauza kuti mtumiki uyu adzayesetsa kucita zotheka pa nchito yace. Sadzacita ulesi pa nchito. Adzagwirira womulemba nchito mokhulupirika pa nthawi yace ya nchito. Mtumiki adzalandira malipiro ace cifukwa ca nchito imene anaigwira mokhulupirika pa kucita nchito yabwino imene womulemba nchito amamulipirira kuti acite.

Mkristu, maka-maka uja amene anasankhidwa ndi mamembala anzace amu mpingo ku udindo wa utumiki, angatenge uthenga wabwino wa Kristu ku malo afakitoli, musitolo, mucinyumba cogwiriramo nchito, mopangira magalimoto, ku manyumba yosungilamo ndalama, ku maofesi ya boma, ndi malo ena anchito. Mtumiki analandira uthenga wabwino wa Kristu, iye amudziwa Yesu Kristu ndipo angalankhule za iye ndi mphamvu. Atumiki mu malo anchito ali okonzekera bwino kunyamula umboni wa Kristu mu malo ace ofunikira kumene milungu ya bodza ipikitsana kuti anthu amene afuna kudza mukudziwa Mulungu woona, Yesu Kristu, amvere milunguyo.

Liu lakulankhulidwa mofatsa la cilimbikitso la kupedzeka kwa Kristu pa nthawi ya mabvuto kucokera ku mtumiki ndiponso wogwira naye nchito pamodzi modyeramo ku nchito kapena pamene mwakhala pansi kupumula pamodzi angatsegule citseko ca mtima wa munthu amene amagwira naye nchito pamodzi amene sali wokhulupirira mwa Yesu Kristu.

Kumbali ina, Mau opanda pace, kulephera kucita nchito yofunikira, kunamizira kudwala kapena maliro kuti mukhale ndi nthawi ya padera yakupumula zidzacititsa kuti ogwira nchito pamodzi ndi mtumikiyo, amene sali okhulupirira, kuti aganizire kuti: Khalidwe lace silisiyana ili cimodzi-modzi ndi ife; anama cabe bodza.

## MTUMIKI KUKHALA CITSANZO PA KUBVOMERA UDINDO WA UTSOGOLERI WA ZA UZIMU

Atumiki ayenera kupezeka ku misonkhano ya atumiki kuthandizira kupereka Mgonero wa Ambuye, kuthandizira pa ubatizo mu njira zina, kuthandizira pa maliro, zikwati, kuthandiza mamembala atsopano ndi kuthandiziranso mu zinthu zina za mndandanda wa utumiki mu mpingo. Mu nchito zopatsidwa ndi zosapatsidwa za utumiki, kodi mpingo ungayembekezere mtumiki kubvomeranso ma udindo ena mu mpingo umene suli wokhuzana ndi nchito ya utumiki? Kodi kukhala "mtumiki" ungakhale mpata wakukana kubvomera nchito zina mu mipingo?

Cipangano catsopano siciyankha mafunso yonse yamene yakhala yali kufunsidwa pa atumiki oyamba. Komatu, pali zinthu zitatu pa atumiki oyamba cimene cipangano catsopano cimanenapo momveka bwino: (1) Khalidwe leni-leni la Cikristu zinagwiritsidwa pa kusankha atumiki oyamba. (2) Nchito kapena utumiki wa atumiki oyamba zinacitika mu mzimu wozicepetsa. (3) Nchito ya atumiki oyamba inali utumiki wa uzimu ndiponso ndi nchito ya utumiki.

Membala aliyense wa mu mpingo adzaziyankhira yekha pa m'mene mpingo umagwiritsira nchito bungwe la atumiki ace. Ngati gulu la atumiki lakhala gulu la kuwerenga pa mpingo, pomwepo ici cabvomerezeka kuti cicitike cifukwa ca ulesi kumbali ya mamembala ya mu mpingo. Ngakhale kuti bungwe la atumiki kugwirizana ndi mbusa akhale atsogoleri pa za uzimu ndi kuthandizira mpingo, mpingo ndi atumiki ayenera kuzindikira kuti nchito yeni-yeni ya atumiki ndi kuthandizira kuzinthu zakuya za uzimu pa mpingo. Ngati mipingo yapatsa munthu udindo wa utumiki cifukwa ca kudziwika kwa munthu kuposa pa cifukwa ca utsogoleri wa Cikristu ndi kacitidwe, pomwepo kufufuzidwa ndi kudziwa kuti ici cotere cacitika m'njira yotani ndipo cakhalirapo ciani.

Pamene munthu wabvomera udindo wa utumiki, abvomera nchito ya kupatsa utsogoleri wa za uzimu. Atumiki ayenera kukhala okonzeka kubvomera maudindo ena mu malo ena amindandanda ya zocitika mu mpingo koposa kukhala cabe mtumiki. Mtumiki ayenera kutumikira monga mphunzitsi wa Sande Sukulu, kupezeka mu komiti kapena makomiti



ocurukirapo ya mu mpingo, angatumikirenso mu maudindo ena mu mpingo monga kukhala wakumpando, msungi cuma, kalembela, kapena woyang'anira wa Sande Sukulu (superintendent). Angakhale mtsogoleri wa bungwe la azibambo kapena wa kumadela ya mpingo. Pamene atumiki akanakutumikira mu madela ena a mndandanda wa utumiki mu mpingo, ndiye kuti utumiki wao uyenera kukhala pa funso lolimba.

Atumiki ayenera kukhala okonzeka kutumikira kuli konse kumene utumiki ndi mphatso za utumiki wao ungagwiritsidwe nchito ndi kumene ufunikira. Ali ndi zofunikira za uzimu zokwanira ndi citsimikizo cogwira nchito bwino. Payenera kukhala kukonzeka kugwira nchito monga kapolo ku mbali ya atumiki mu mpingo kuli konse kumene utsogoleri wao ungafunike.

Kukula kwa uzimu kwa asosiyeshoni ndi Konveshoni uli maka-maka wogwirizana ndi utsogoleri woyenera wopezeka mu mipingo. Kopanda utsogoleri wabwino mu mpingo, zonse ndi kubvutika - mpingo, asosiyeshoni ndi Konveshoni. Atumiki ayenera kukhala patsogolo pa kupatsa citsanzo ku kukula mu Cikristu pa kupatsa utsogoleri wofunikira wa Cikristu mu mndandanda wa utumiki wa za uzimu mu mpingo.